Matenda a Chitopa ndi Katemera wa Nkhuku Kumadera a Kumidzi

Buku Lophunzitsira

Rural Poultry Centre
Malawi

Rural Poultry Centre
PO Box 81
Likuni
Malawi

http://www.ruralpoultrymalawi.org

KYEEMA FOUNDATION

Australian Aid

Chithokozo ndi Chidziwitso

Buku lophunzitsirali linalembedwa pongwiritsira ntchito upangiri ochokera m'mabungwe osiyanasiyana monga ACIAR ndi SSLLP mwaena.

Zazikulu za bukuli zinachokera muchidziwitso kudzanso zipangizo za bungwe la maziko a Kyeema ndi nthambi yake ya International Rural Poultry Centre monga muzu weniweni.

Bukuli linatanthauzidwa ndi Luka Tumbwe mothandizana ndi Andrew Chimalizeni.

Thandizo lomaliza linapatsidwa ndi Boma la Australia limene tiyenera kulithokozanso kwakukulu. Ntchito ya maphunziro a nkhuku zam'midzi m'Malawi tere ndi thandizo la bomali podutsira m'bungwe lalikulu la Kyeema.

Buku limeneri lalembedwa ndi cholinga chothandiza alangizi kuti akathe kuphunzitsa alangizi a m'midzi pakangwiritsidwe ntchito kakatemera wa I-2 amene amateteza nthenda ya chitopa. Sirinalembedwa mozama kwambiri koma momveka bwinobwino kuti ophunzitsidwawo kumidzi akazindikire ndi kumvetsa mosabvuta. Motero ndiro buku lophweka ndi lolembedwa mowumba mkota koma mwaukadaulo zedi.

Aliyense mlangizi wa kumidzi amene waphunzitsidwa pongwiritsa ntchito bukuli apatsidwe lake ndicholinga chakuti asakaiwale pomakawerenganso.

Ndizotheka kupezanso bukuli pa RPC website pa:

http://www.ruralpoultrymalawi.org

Zamkatimu

Gawo 1: Za Matenda a Chitopa 1

Gawo 2: Katemera wa Chitopa 6

Gawo 3: M'mene tingakonzekere za kaperekedwe ka katemera ... 9

Gawo 4: Zokhudza katemera wa I-2 16

Gawo 5: Mafunso ndi mayankho ake 20

Kasungidwe ka Marekodi a Katemera wa Chitopa 22

Kayendetsedwe ka Katemera wa Chitopa 23

Ndondomeko ya ntchito mwezi uli wonse wa pa chaka 25

Gawo 1: Za Matenda a Chitopa



Matenda a nkhuku alipo ambiri. Ena mwayiwo ndiwodetsa nkhawa, chifukwa amapha nkhuku zambiri. Koma zokambirana zathu zalero zikhudza nthenda imodzi yokha. Nthendayi ndi chitopa. Maina ena ndi "chideru" kapena "chipumphu" kapena "dzoye". Iyi ndi nthenda ya nkhuku yowopysa zedi kuno ku Malawi.
Palibenso matenda ena omwe amapha nkhuku koposa a chitopa. Panopa tifuna tiphunzire za chitopa ndi kupewa kwake pogwiritsa ntchito katemera.

Chitopa ndi chiyani?

Chitopa ndi matenda a nkhuku ndi mbalame zina. Amabwera mu nyengo zosiyanasiyana, kamodzi kapena katatu pa chaka. Amapha nkhuku zambiri, koma zina zochepa zimatha kupulumuka. Nthendayi imabwera ndikupita mobwerezabwereza. Anthu akumidzi amayidziwa nthendayi ndi zizindikiro zake zomwe.

Chimayambitsa chitopa ndi chiani?

Choyambitsa matenda a chitopa ndi kachilombo kakang'ono kwambiri kotchedwa vailasi. Pali mitundu yosiyanasiyana ya ma vailasi, koma ndi mtundu umodzi okha umene umayambitsa chitopa. Popanda kachilomboka chitopa sichingapezeke.

Nkofunika bwanji kudziwa za chitopa?

Chitopa ndi choopysa zedi. Ndi nthenda imene imapha nkhuku zambiri ku midzi m'dziko muno. Matenda ena kapena zolusa zina zikhonza kupha nkhuku koma sikawirikawiri monga chimachitira chitopa.

Nthendayi imabwera bwanji?

Kachilombo kachitopa kakalowa m'thupi la nkhuku, imayamba kudwala. Kachilomboka kamachokera ku mbalame zina zodwala. Kawirikawiri chitopa chimabwera chifukwa cha mavailasi ochokera ku nkhuku zodwala kale nthendayi. Nthawi zina mbalame za kutchire ndi zimene zimabweretsa ma vailasiwa ku nkhuku zathu. Zinanso zimene zimanyamula mavailasi a nthendayi ndi magalimoto, mphepo, ziwiya ndi ife anthu oyendayenda.

Zimatani kavailasi kakalowa m'thupi la nkhuku kuti iyambe kudwala?

Pamatenga masiku ochepa mwina sabata kachilombo katalowa m'thupi la nkhuku kuti iyambe kudwala...



Poyamba kavailasi kamalowa m'thupi la nkhuku.



Pambuyo pake tizilombo timayamba kuchulukana pang'ono pang'ono.

Panthawiyi nkhuku sisonyeza zizindikiro zodwala.



Tizilombo tikachulukana kwambiri m'thupi la nkhuku imayamba kupatsirana ndi zinzake kudzera njira yopumilana ndi zitosi.

Apa ndiye kuti nkhuku yayamba kudwala. Ikhoza kufalitsa ma vailasi ndi matendawa ku nkhuku zina.



Tizilomboti timapitirirabe kuchulukana ndi kumafalikira ku nkhuku zambiri kudzera mumpweya ndi zitosi.

Tsopano nkhuku yadwala kwambiri ndipo ikufa.

Zizindikiro za chitopa?

Timaona nkhuku yovuvumala ndi nthenga zonyankhalala.

Nkhuku zambiri zimaoneka zodwala ndipo zimafa mowirikiza.



Nthawi zina, tizilomboti timakhudza matumbo a nkhuku. Ndiye, timaona kuti nkhuku imatulutsa zitosi za gilini.

Nthawi zina, timaona kuti nkhuku zimayenda mopeyukapeyuka ngati yaledzera ndi kuonetsa makosi opotoka.

Apa ndiye kuti tizilombo tafika ku bongo la nkhuku.

Matendawa akafika povuta kwambiri, nkhuku zonse zimafa. Nthawi zina, nkhuku zambili zimafa koma zina zimakhoza kupulumuka.

Tingachize bwanji chitopa?

Poyambirira tizindikire chinthu chimodzi, kuti kuchiza ndi kutchinjiriza matenda ndi zinthu ziwiri zosiyana. Anthu ambili samadziwa izi.

- **Kuchiza** ndi kuchiritsa chiweto chodwala.
- **Kutchinjiriza** ndi kuteteza chiweto kuti chisadwale.

Palibe mankhwala a matenda a chitopa. Pamene matenda agwa/alowa m'mudzi, nkhuku zambiri zimafa pokhapokha ngati zinalandira katemera. Ngati matendawa agwira nkhuku palibe mankhwala amene angachize nkhukuzi.

Anthu ambiri amakhulupirira kuti pali mankhwala a zitsamba ochiza nthendayi, koma izi sizoona. Nkhuku sizichira ndipo zimafabe mowirikiza.

Tingapewe bwanji chitopa?

Njira yodalirika popewa chitopa ku nkhuku za kumidzi, ndi katemera. Njilayi ndiyosavuta komanso yosalowa m'thumba.

Pali mitundu yambiri ya katemera wa chitopa, koma pano tifuna tiphunzire za mtundu umodzi wa I-2.

Central Veterinary Laboratory Mw
I-2 Newcastle Disease Live Vaccine
300 doses Store at 4-8°C
Administer by eye drop
Batch No. 999/999 Exp Date: 06/2020
For animal use only

Gawo 2: Katemera wa Chitopa

Katemera wa chitopa amateteza bwanji nkhuku?

Poyamba tiyeni tione chitsanzo cha nkhuku yodwala chitopa...

Ngati kachirombo koyambitsa matenda a chitopa kalowa m'thupi la nkhuku, nkhukuyi imaonetsa zizindikiro zodwala pamasiku awiri. Choncho ikhoza kufa pa masiku awiri ena otsatira.



Ngati nkhuku siifa, imachira, ndipo kuti m'thupi mwake mwapangidwa asitikali ogonjetsa matendawa.

Asitikaliwa amapha tizilombo tonse toyambitsa matendawa ndiye nkhuku imachila. Kupanga asitikali oteteza kumachitika mkati mwa mulungu umodzi.



Katemera wa chitopa amagwira ntchito yodzidzimutsa thupi la nkhuku ndipo limapanga asitikali ogonjetsa matendawa. Koma katemerayu samadwalitsa nkhuku.



Pa sabata imodzi kuchokera pa tsiku limene katamerayu anaperekedwa, nkhuku imapanga asitikali amphamvu ogonjetsa matendawa.

Sabata imodzi

⬇



Nkhuku yomwe yalandira katemerayu simadwala matendawa, chifukwa ili ndi chitetezo chokwanira. Imakhalabe ndi asitikali amphamvu kwa miyezi yochepa.

Pamatenga pafupifupi sabata kuti chitetezo chikhazikike m'thupi la nkhuku

Katemera wa chitopa sabweretsa chitetezo nthawi yomweyo. Pamatenga pafupifupi sabata kuti chitetezo chikhazikike mokwanira m'thupi la nkhuku. Ngati mwapereka katemera wa chitopa ku nkhuku yodwala imafa msanga.

Apa taona kusiyana kwa kuchiza matenda ndi kuteteza matenda m'njira ya katemera. Sitingathe kuchiza nkhuku ndi katemera.

- Ngati mupatsa katemerayu ku nkhuku yodwala kale chitopa, imafa.
- Ngati mupereka katemera ku nkhuku chitopa ndikubwera pasanathe sabata, nkhuku zikhonza kufabe.
- Ngati chitopa chitabwera patatha sabata katemerayu ataperekedwa pali mwayi waukulu kuti nkhuku zikhonza kupulumuka.

Katemera ayenera kubwerezedwe miyezi inayi iliyonse

Pali zifukwa ziwiri izi zobwerezera katemerayu pamiyezi inayi iliyonse.

Choyamba, chitetezo chimatsika pakamapita nthawi. Pakapita miyezi inai, chitetezo chimatsikilatu. Ndiye tiyenera kutemeranso nkhuku.

Chachiwiri, anapiye amene abadwa titatemera kale ayenera kulandira katemera asanadwale.

March, July ndi November ndiyo miyezi yobvomerekezeka kupereka katemerayu.

Katemera wa I-2 ndi wa chitopa chokha, osati matenda ena ali onse

Timadziwa za katemera wa ana athu kuti katemerayu amateteza nthenda imodzi basi osati matenda ena onse. Chimodzimodzi katemera wa I-2 amateteza chitopa chokha.

Nkhuku zimene zalandira katemera wa chitopa zitha kufa ndi matenda ena omwe amagwira nkhuku, osati chitopa.

Katemera wa I-2 ndi wodalirika

Katemera woteteza ku matenda a chideru sioopsa ayi. Ngati nkhuku zidwala kapena kufa zitangolandira katemerayu ndiye kuti zadwala ndi kufa ndi matenda ena osati katemerayu.

Katemera wa I-2 samasintha chilichonse m'thupi la nkhuku, ngakhale kukoma kwa nyama yake.

Palibe bvuto kudya nkhuku imene yalandira katemerayu nthawi yomweyo.

Ngakhale mazira ankhuku yolandira katemerayu tikhonza kudya, ndiponso amatha kukonkhomora anapiye bwinobwino.

Osapereka katemera ku nkhuku zodwala

Tipatse katemerayu nkhuku zokhazo zomwe zili za thanzi, pazifukwa izi:

Katemerayu sagwira ntchito moyenerera ngati tipereka ku nkhuku zodwala kale, chifukwa zimakhala zofoowoka kale. Ngathi thupi la nkhuku ndi lofooka asilikali ogonjetsa matenda a chitopa amakhalanso ofooka.

Taphunzira kuti nkhuku zodwala kale zikalandiranso katemera zimafa, ndipo zikachitika izi mlimi amadandaura kuti mlangizi wamphera nkhuku zake pozipatsa katemerayu. Patsogolo pake salolanso kuti nkhuku zake zilandirenso katemera, ndipo amakopanso anzake powauza kuti katemera ndiwoipa. Pamapeto pake alimi amataya chikhulupiriro chawo pa za katemerayu.

Pazifukwa izi tiyeni **tisapereke** katemera ku nkhuku zodwala, pokana kukhumudwitsa alimi. Tipereke katemera ku nkhuku za thanzi zokha.

Gawo 3: M’mene tingakonzekere za kaperekedwe ka katemera

Mkofunikira kukonzekera tisanakapereke katemera m'midzi yomwe tikagwireko ntchitoyi. Ndi bwino alimi adziwe za ntchitoyi ndi nthawi yodzaperekera katemera. Izi zimathandiza kuti ntchito ya katemera iyende bwino.

Kukonzekera kwa ntchitoyi pafunika kuwadziwitsa, kuwaphunzitsa eni a nkhuku ndi kudziwa chiwerengera cha nkhuku m'mudzimo. Izi zidzatithandiza kudziwa kuchuluka kwa katemera amene adzafunika.

Kufalitsa ndi kudziwitsa

Tsiku la katemera lisanafike, mlangizi apite ku midzi yomwe akagwire ntchitoyi, ndi kuwadziwitsa alimi za ntchitoyi ndi nthawi, komanso kuwaphunzitsa za ubwino wa katemerayu ndi kuwapatsa mwayi ofunsa zimene afuna kudziwa.

Tiwauzenso alimi za mtengo wakatemera pa nkhuku iliyonse.

Sikofunikira kuti alimi adziwe zonse za m'bukuli. Komabe ayenera adziwe izi:

Zomwe alimi ayenera kudziwa

1. Chitopa ndi matenda oopysa zedi, amene akhoza kupewedwa pogwiritsa ntchito katemera wa I-2. Katemerayu aperekedwe pakatha miyezi inayi iliyonse.
2. Palibe mankhwala ochiza chitopa. Chikafika chitopa pa mudzi, nkhuku zambiri zimafa, pokhapokha ngati zinalandirapo katemera kale.
3. Katemera sachiza chitopa, koma amatchinjiriza chitopa ku nkhuku zathu ndi kuzipatsa chitetezo asanabwere matendawa kwathu.
4. Katemera sagwira ntchito nthawi yomweyo. Chitetezo chimabwera pangonopangono kufikira sabata, ndipo chimapitirira kuteteza nkhuku kwa miyezi inayi.
5. Alimi asamadikire chitopa chifike. Chifukwa akatero nkhuku zawo zidzafabe zambiri pokhapokha ngati zinalandirapo kale katemera.
6. Ngati alangizi a ku mudzi simuyenera kupereka katemera ku nkhuku zodwala. Ngati nkhuku zikudwala, thupi lake limakhala lofooka, ndiye katemera sangathe kugwira bwino ntchito m'thupi lofooka. Ndiye nkhuku zimafabe. Ngati atemera nkhuku zodwala ndi kufa mlimi adzataya chikhulupiliro kwa alangizi aja. Pazifukwa izi mudzikana kupereka katemera ku nkhuku zodwala.
7. Alimi adziwe kuti katemera wa chitopa ndi wa nkhuku iliyonse yaing'ono kapena yaikulu. Ngati katemera angaperekedwe kwa nkhuku zochepa, zotsalazo zifabe.

Ndibwino kukhoma mapepala azidziwitso m'malo onse amene katemera akaperekedwe. Onani chitsanzo pa Apendekisi 3. Izi zionetse mudzi, tsiku, ndi mtengo wa katemera pa nkhuku iliyonse.

Kalembera

Mlangizi aliyense ayenera kudziwa kuchuluka kwa katemera amene akufunika mogwirizana ndi chiwengero cha nkhuku kudelako.

Mlangizi ayenera kufunsa kwa mlimi aliyense m'mudzi pofuna kudziwa chiwerengero chenicheni cha nkhuku zoyenera kulandira katemera. Izi zilembedwe m'buku monga momwe talembera mu Apendekisi 1.

Zikatha izi tiumbe mkota chiwerengero chonse cha nkhuku zofunika kutemeledwa.

Kabotolo kamodzi ka katemera kamasunga ma dontho 300 (mazana atatu). Nthawi zina, mlangizi amatha kubwereza kupereka ma dontho awiri akatemera ku nkhuku pazifukwa zina. Motero timayerekeza kuti botololi limakwana nkhuku 250. Choncho tingathe kuwerenga chiwerengero cha ma botolo ofunika. Pa nkhuku 250, pafunika botolo limodzi.

Kukonzekera katemera kumidzi - Kachitidwe ka business.



Mlangizi aliyense wa katemera wa chitopa ayenera kudziwa kukonza ndondomeko ya biziness kuti ndondomeko ya katemera ikhale yokhazikika. Kutemera wa chitopa atha kukhala bizinesi ya phindu. Muyenera kudziwa kuwerengetsera cholowa. Chitsanzo:

Ndalama zopangidwa:

Nkhuku zimene tabaya A	X	Mtengo wa katemera pa nkhuku imodzi B	=	Ndalama zomwe mwalandira zonse pamodzi. C

Zogula:

Mtengo wa katemera D	+	Zogula zina monga ulendo komanso phoso E	=	Ndalama zonse zomwe mwalowetsa F

Phindu:

Ndalama zotsala m'thumba mwanu G	=	Ndalama zonse zomwe mwalandira C	-	Ndalama zonse zomwe mwalowetsa F

Chitsanzo (ndi kupitiliza kuyeselera):

A	Chiwerengero cha nkhuku zomwe zalandira katemera	250		
B	Mtengo wa katemera pa nkhuku imodzi	K40		
C	Ndalama zomwe mwalandira zonse pamodzi	K10,000		
D	Mtengo ogulira katemera	K3,000		
E	Zina zomwe mwalowetsa mu bizinesi - chitsanzo ndalama zomwe mwagwiritsa ntchito pa mayendedwe ndo phoso.	K500		
F	Ndalama zonse zomwe mwalowetsa.	K3,500		
G	Phindu - Ndalama zotsala mnthumba mwanu (C - F)	K6,500		

Pali nthawi yaitali bwanji ?

Alangizi ambiri akumidzi okhazikika m'ntchito yopereka katemera amatemera nkhuku 300 pakati pa tsiku limodzi kapena masiku awiri. Ntchitoyi alangiziwa samayigwira tsiku lonse chifukwa katemerayu amaperekedwa m'mawa nkhuku zisanatulutsidwe. Mwachidule, phindu la K6,500 m'chitsanzo chomwe taperekachi limapezedwa pantchito yamaola ochepa. Ndi ntchito inanso iti yomwe ingakupatseni phindu lotere m'maola ochepa a masiku awiri?

Sungani ndalama zogulira katemera padera.

Ndikofunika kwambiri kuika padera ndalama zogulira katemera. Ndalama izi zizipezeka pamene mwazifuna kuti mukagule katemera.

Dziwani izi:

- Ngati palibe ndalama, palibe katemera
- Ngati palibe katemera, palibe ntchito ya kutemera nkhuku
- Ngati palibe nkhuku, palibe phindu
- Ngati sitingatemere nkhuku, zambiri nkhukuzo zidzafa ndithu
- Ngati nkhuku zochuluka zafa, ndiye kuti mlimi ali paumphawi wa njala ndi ndalama.

Alimi ayenera kulipira katemera

Ndikofunika kwambiri kuti alimi amene ali ndi nkhuku azilipira kuti nkhuku zawo zilandire katemera chifukwa ngati sangalipire, mlangizi akagula bwanji katamera wina? Alimi akapanda kulipira, alangizi sadzapeza phindu ndipo chidwi chopitiliza ntchito yawo chidzawathera. Izi zitanthauza kuti nkhuku zambiri sizidzatetezedwa ku matenda a chitopa.

M'madera otere amene alimi amachita ukamberembere, atsogoleri komanso mafumu akuyenera kuuza anthu a m'midzi mwao kuti khalidwe lotere liika chiopsezo pa kupitilira kwa ndondomeko ya katemera ku dera lawo. Nanga ndibwino kukhala ndi mudzi opanda nkhuku? Mafumu ndi atsogoleri ayenera kuzindikira kufunika kwa katemera. Pamene pali kothekera, mafumu ayenera kuchita nawo maphunziro a alangizi a katemera komaso azipezeka m'misokhano ya kalondolondo wa m'mene ntchito ya katemera ikuyendera ku madera awo.

Kukhazikitsa magulu.

Pali zifukwa zambiri zakuti alangizi okhala moyandikana azikhalikitsa ku magulu potengera dera (EPA) lomwe ali. M'magulu, alangizi anatha kukambirana ndikumapeza njira zothetsera mavuto awo, kusonkherana ndalama zokagula katemera, kulandira mathandizo kwa alangizi aboma kapena amabungwe, ndiponso kukonza ndi kulunzanitsa ndondomeko ya katemera. Tsono mungakonze bwanji magulu?

Gulu liyenera kukonza msonkhano wa alangizi onse omwe angakhale ma membala. Pa msonkhanotere, alangizi akhazikitse malamulo oyendetsera gulu lawo komanso oyendetsera ndondomeko ya kasankhidwe ka wa pampando, mlembi, komanso nsungi chuma. Gulu liyenera kusankhanso wachiwiri wa pampando komaso wachiwiri mlembi.

Gulu liyenera kusankhanso membala okhulupirika komanso odalilika yemwe m'nthawi yoyenera azizatolera ndalama kwa ma membala ndicholinga chokagula katemera m'malo mwa ma membala onse. Mugawo likubwerali, tiona m'mene njira yokonza magulu ingathandizire kuchepetsa ndalama zomwe alangizi amalowetsa mu bizinesi ya katemera.

Gulu liyenera kumasonkhana mwezi uliwonse. Ndikoyenera kukhazikitsa tsiku loikika la msonkhano kuti alangizi asamaiwale. Ma membala ayenera kuonetsetsa kuti akubwera ku misonkhano ya gulu. Gulu lililonse lizikhazikitsa malamulo ndi cholinga choonetsetsa kuti membala aliyense azipezeka.

Kugula katemera

Katemera wachitopa wa I-2 amagulidwa ku Central Veterinary Laboratory ku Lilongwe. Pakadali pano, mtengo wa botolo la katemera (lomwe limatemera nkhuku 300) uli pa K1,100. Alangizi ambiri amangofuna botolo limodzi kapena awiri kukatemera nkhuku zonse za ku dera lawo. Kupita ku Lilongwe kukagula botolo limodzi kapena awiri basi kungasakaze ndalama chabe chifukwa cha phoso ndi mayendedwe. Ngakhale zili chomwechi, m'magulu, titha kusonkherana ndalama kuti tikagule katemera pamodzi. Izi zidzapangitsa phindu lomwe alangizi amapeza kukhala lalikulu. Pano pali chitsanzo ichi kuonetsa zimenezi. M'chitsanzochi, tisiyantisa ndondomeko ziwiri:

- Mlangizi m'modzi apita kuchokera ku Mchinji kupita ku Lilongwe kukagula mabotolo awiri a katemera;
- Gulu la alimi 10 asonkherana ndalama natuma mlangizi m'modzi kukagula ma botolo 15 a katemera.

Chitsanzo chotsatirachi, tisiyanitsa ndalama zimene alangizi amalowetsa akapita paokha kukagula katemera ku Lilongwe kuchokera ku Mchinji ndi ndalama zomwe gulu la alimi 10 limalowetsa potuma m'modzi kukagula ma botolo 15 akatemera. Taikanso ma bokosi opanda kanthu mu chitsanzochi kuti muthe kupitiriza kuyesererapo.

Katundu	Kugula mabotolo 2 payekha	Kugula mabotolo 15 pa gulu	Chitsanzo chanu
Mtengo wa mayendedwe MC-LL-MC	8,000	8,000	
Mtengo wa mayendedwe mu LL	1,000	1,000	
Mtengo wa chakudya/ phoso	1,500	1,500	
Mtengo wa katemera ku CVL	2,200	16,5000	
Ndalama zonse zofunika	12,700	27,000	
Nambala ya mabotolo akatemera omwe agulidwa	2	15	
Mtengo wa katemera wa botolo 1	**6,350**	**1,800**	

Tikhoza kuona kuchokera mu chitsanzochi ubwino wopangira zinthu pagulu. Ngati mlangizi apita kukagula katemera payekha mabotolo 2 ku Lilongwe, ndalama zonse zikukwana K6,350 pa botolo limodzi la katemera kuphatikizapo mtengo was mayendedwe ndi phoso. Pamene ngati gulu litumiza munthu m'modzi kukagula mabotolo 15 akatemera, ndalama zonse zikukwana K1,800 pa botolo limodzi kuphatikizapo mtengo wa mayendedwe ndi phoso.

Inde, pali enanso amene amagulitsa katemerayu m'dera lanu pa mitengo ya pakati pa K3,000-K4,000, m'malo monga Kamwendo kapena paboma.

Nthawi iliyonse pamene mufuna kugula katemera, muzionetsetsa zinthu ziwiri izi:

- Muziyang'ana katemera adzatha mphamvu mwezi uti.
- Muzionetsetsa kuti wina sanatsegulepo chotsekera cha botolo lakatemera.

Gawo 4: Zokhudza katemera wa I-2

Pano tiphunzira za katemera wa I-2 amene alipo kuno kwathu ku Malawi. Komanso amagwirizana ndi nkhuku za muno m'Malawi

Momwe tingasungire katemera wa I-2

Pali njira zosavuta ngati izi:

- Sungani katemerayi pa malo ozizira nthawi zonse.
- Mukhonza kusunganso mu fuliji, koma osaika m'malo oumitsila.
- Katemera asaundane.
- Osasunga katemera pa dzuwa.
- Gwiritsani ntchito katemerayu pamasiku awiri kapena atatu, mukachotsa mu fuliji.

Momwe tinganyamulire katemera wa I-2

Chithunzichi chikusonyeza kadengu kabwino kunyamulira katemera kumidzi. Timakulunga katamerayu m'kansalu konyowa ndi kuika m'kadengu.

Kadenguka kamalora mpweya kuti uzidutsa. Zimene zimapangitsa katemera akhalebe ozizira.

Ngati munyamula katemera kukasunga m'fuliji, gwiritsani ntchito komtena yokhala ndi madzi ouma (ice).

Kakonzedwe ka filiji ya kumudzi.

Alangizi ayenera kusunga katemera pa malo ozizira, monga mu filiji nthawi zonse. Alimi ambiri filiji ikhoza kutivuta kupeza ndipo chifukwa cha ichi tiphunzira kukonza filiji yakumudzi yosalowa m'nthumba pogwiritsa ntchito zipangizo zopezeka m'madera athu. Tifunika tikhale ndi:

- Malo a mthunzi m'nyumba pomwe mpweya umadutsa bwino;
- Tipeze kam'khate ka kamonjo - kunena kamtsuko komwe simunaphikiremo kalikonse komwe kamalola kuti madzi azichucha/azikha pang'onopang'ono;
- Mafuwa kapena njerwa zoti tikhazikepo mtsuko;
- Madzi komanso mchenga.

M'musimu taonetsa njira ziwiri za m'mene tingasungire katemera. Njirazi zimagwira bwino ntchito m'masiku otentha- njirazi sizidalilika m'masiku a mvula. Mpweya omwe ukuzungulira umachititsa kuti chinyezi chiziuluka kuchoka mumchenga kapena madzi ndipo izi zimapangitsa kuti malo omwe tasunga katemera akhale ozizira.



Kugwiritsa ntchito katemera wa I-2



Pangirani katemera wanu pa mthunzi.

Nkhuku yaikulu ndi yaing'ono, zonse zilandire katemera.

Gwedezani botolo la katemera poyamba. Thirani dontho limodzi m'diso limodzi la nkhuku iliyonse. Ngati muthira madonto ambili, palibe bvuto. Gwirani botololi molunjikitsa ngati liliri mu chithunzichi. Ngati simungagwire molunjikitsa botololi, mudzataya madontho ochulika akatemerayu.

Onetsetsani kuti botolo lakatemera lisakhudze ndi diso kapena khungu lankhuku. Komanso botololo likhale laukhondo ndithu. Pakati pabotolo lakatemera ndi diso lankhuku pazikhala mpata otalikirana 2-3 cm.

Kumakhala kwabwino kuti mlimi agwire miyendo ndi mapiko a nkhuku yake. Ndipo mlangizi agwire mutu monga chitsanzo taperekachi. Potero tidzapewa kutaya madontho ochuluka.

Werengani chiwerengo cha nkhuku zotemeredwa m'buku lanu, monga yooneka mu Apendekisi 1.

Botolo limodzi limasunga madontho 300 koma mwina ena amatayika pogwiritsa ntchito ndiye timatengera pa madontho 250. Utasamalitsa osatayapo madonthowa ena ndiye amatemera nkhuku 300 pa botolo limodzi.

Sibwino kumasonkhanitsa nkhuku zambiri m'midzi yosiyana pamodzi chifuka nkhuku zina zikhoza kukhala zodwala ndi kufalitsa matendawo ku za m'midzi ina. Chifukwa cha kupewa kupatsirana matenda nkukuzi, mlangizi apereke katemera pa mudzi umodzi ndi kusamba m'manja ndi sopo asanapite kumudzi wina.

Mlimi aliyense azidziwitsidwa nthawi zonse kuti chitetezo m'thupi la nkhuku chimayamba pakapita sabata imodzi zitalandira katemera, ndipo chimakhala mpaka miyezi inayi ina.

Mlimi akumbutsidwenso kuti katemerayu sioopysa ayi motero akhoza kudya nkhuku imene yalandira katemera kumene. Chimodzimodzi mazira ake palibe bvuto kudya.

Tayani mosamala mabotolo opanda kanthu

Onetsetsani kuti pamene mwamaliza kupereka katemera, muyenera mutaye botolo lopanda kanthu mu chimbudzi chokumba. Chifukwa chiani? M'mbuyomu, akathyali ena akhala akumatola mabotolo akatemera opanda kanthu ndikumaikamo madzi ndi kumanamiza alimi kuti iwo ndi alangizi akatemera wa chitopa. Iwo amawalipitsa alimi pamene ndi katemera wabodza. Izi zitachitika m'dera lanu, chingachitike ndi chiani? Patsogola chitopa chikabwera, nkhuku zidzafa. Eni nkhuku adzaganiza chiani? Iwo adzaganiza kuti katemera wanu wa chitopa sagwira ntchito. Inu mukabwera ndi katemera weniweni, sadzalolo kutemera nkhuku zawo. Kumbukirani:

- Ngati palibe ndalama, palibe katemera
- Ngati palibe katemera, palibe ntchito ya kutemera nkhuku
- Ngati palibe nkhuku, palibe phindu
- Ngati sitingatemere nkhuku, zambiri nkhukuzo zidzafa ndithu
- Ngati nkhuku zochuluka zafa, ndiye kuti mlimi ali paumphawi wa njala ndi ndalama.

Gawo 5: Mafunso ndi mayankho ake

Mafunso ena amene alimi ankhuku angafunse ndi mayankho ake

Mlangizi ndi amene amakhala kwambiri ndi alimi ankhukuwa motero ayenera kudziwa zambiri za katemera wa chitopa cha nkhuku. Alimi ena sakumbukira zoperekanso katemerayu ku nkhuku zawo mpaka matenda atafika ndiye amafuna thandizo. Ndipo alimi ena amakhala kuti alibe makobidi olipira nkhuku zawo zikamatemeredwa. Nthawi zina alimi amayesetsa kupeza kachifukwa kena kalikonse ndi cholinga chofuna kuipsa ntchito ya katemerayu.

Pano taika mfundo zina zimene zingathandize poyankha mafunso ena amene alimiwa amakonda kufunsa.

1. Zikomo kwambiri popereka katemera kunkhuku zanga lero koma moti sizidwalanso chitopa?

Zoyenera kuyankha:

> *Sizotetezedwa panopa ayi koma pakatha mlungu umodzi. Katemerayu amagwira ntchito pang'onopang'ono m'thupi la nkhuku kuti chitetezo chichuluke. Motero zimatenga sabata yanthunthu kuti chitetezo chikhale cha mphamvu. Pamenepo ndizotetezedwa ku chitopa. Kumbukilani kuperekanso katemerayu ku nkhukuzi komanso anapiye patsogolo pano pakapita miyezi inayi.*

2. Nkhuku zanga zikufa ndi chitopa kodi mungandithandize bwanji?

> *Palibe njira iliyonse imene ine kapena wina aliyense angathe kukuthandizani pamene matenda ayamba kale. Chitopa chilibe mankhwala. Inu dikirani chabe kuti chipite tsono patsogolo pake mudzakumbukile kuzipatsa nkhuku zanu katemera wa chitopa.*

3. Koma nkhuku zanga zikufa kodi simungapereke katemera kuti zileke kufa?

> *Katemera simankhwala ochizila chitopa ayi, kapena sangathe kuletsa kufa kwa nkhuku, chitopa chikafika m'mudzi. Timapereka katemerayu kunkhuku zathanzi zokha zimene zilibe chitopa. Palibe mankhwala a chitopa.*

4. Nkhuku zanga zangoyamba kumene kudwala; ndichifukwa chiyani mukukana kudzipasa katemera?

Nkhuku zanu zikudwala ndipo matupi awo ndi ofooka, motero ngati zitapatsidwa katemera chitetezo chake chikhalabe chofooka. Nkhuku zipitirira kufooka osathandizika. Nkhuku zathanzi ndi zimene zikapatsidwa katemera, chitetezo chake m'thupi chimakhala champhamvu. Tiyeni tizipatse nkhuku katemera pamene sizinadwale.

5. Nditani nanga popeza ndalama ndilibe zolipira katemera?

Ngati muli ndi nkhuku khumi, bwanji mugulitseko imodzi. Mukatero mukhala ndi ndalama zolipira katemerayu ndipo mupulumutsa zotsalazi ku chitopa. Pangani chiganizo nokha kuti nkhuku zonse zife ndi chitopa kapena mugulitse imodzi ndi kupulumutsa zisanu ndi zinayi.

6. Katemera wanu anapha nkhuku zanga mutangozipatsa basi zonse kufa.

Katemera alibe bvuto ayi ndipo sangathe kupha nkhuku. Pamatenga sabata imodzi kuti katemera ayambe kugwira ntchito m'thupi lankhuku.Ngati nkhuku zanu zinafa zitangolandira katemera, ndiye kuti zinali zodwala kale chitopa kapena nthenda ina.

7. Katemera wanu sanagwire ntchito chifukwa nkhuku zanga zinafa pamasabata ochepa mutangozipatsa katemera.

Palibe bvuto lililonse ndi katemerayu. Amapereka chitetezo chokwanira pa matenda a chitopa. Pamatenga mulungu umodzi kuti nkhuku zotemeredwa zikhale ndi chitetezo chokwana cha m'thupi. Ndipo chitetezo chimenechi chimatha mphamvu pakapita miyezi inayi. Ngati nkhuku zanu zinafa masabata angapo zitalandira katemera ndiye kuti zinafa ndi matenda ena. Katemerayu amateteza nkhuku kumatenda a chitopa okha basi. Nkhuku zimakhoza kufa ndi matenda ena. Katamerayu sangathe kuletsa kufako.

Apendekisi 1

Kasungidwe ka Marekodi a Katemera wa Chitopa

Dzina la mlangizi: _____

Tsiku: _____

Dzina la Mlimi	Mudzi	Ali ndi nkhuku zingati?	Nkhuku zingati zotemeredwa	Ndalama zaperekedwa
1)				
2)				
3)				
4)				
5)				
6)				
7)				
8)				
9)				
10)				
11)				
12)				
13)				
14)				
15)				
16)				
17)				
18)				
19)				
20)				

Apendekisi 2

Kayendetsedwe ka Katemera wa Chitopa*

Dzina la mlangizi: _____

Tsiku (masiku) la kutemera: _____

Mabotolo a katemera poyamba kutemera: _____

Mabotolo a katemera otsala pomaliza kutemera: _____

Mudzi	Nkhuku zingati zilipo?	Nkhuku zingati zotemeredwa?
Zonse pamodzi:		

* Mukamaliza kutemera nkhukuzo, tumizani fomu iri kwa alangizi a za vetenari kapena alangizi ena a za ulimi.

Apendekisi 3

TETEZANI NKHUKU ZANU KU

CHITOPA

PEREKANI KATEMERA KU NKHUKU ZANU KUTI MUPEWE CHITOPA

Tidzapereka katamera wa chitopa motere:

Mudzi:	
Tsiku:	
Mtengo wankhuku imodzi:	

ZIKOMO

Apendekisi 4

Ndondomeko ya ntchito mwezi uli wonse wa pa chaka

Janyuari	Feburuari	Malichi	Epulo
Meyi	Juni	Julayi	Ogasiti
Sepitembala	Okotobala	Novembala	Disembala
Kuwerenga nkhuku. Kuitanitsa katemera	Kupezeka kwa katemera ku midzi	Kutemera nkhuku	Kulondola ndondomeko ya katemera m'mene anayendera